10. Mmalo mwa golidi wa Mfumu tikhoza kukhala omvera. Pamene ife timvera Yesu timaonetsa kuti Iye ndi mfumu. Mphatso ya anthu anzeru ya golidi imatikumbutsa ife za kumvera.

Mphatso yachiŵiri ya anthu anzeru inali libano. Libano ndi tinthu toumitsidwa timene timachotsedwa kumitengo ya mtundu wina. Pamene ali kutenthedwa amapereka pfungo lokoma. Chifukwa cha funso labwino limeneli, Ayuda anali kuotcha libano m'kachisi. Ili linali gawo limodzi lopembedza Mulungu. Libano anali mphatso ya kwa Mulungu.

Pamene anthu anzeruŵa anapereka libano, kodi iwo anaonetsa chiyani za Yesu?

______________________________________________

==================================================================

11. Iwo anali kuonetsa kuti Yesu anali Mulungu. Yesu ndi mfumu, koma Iye ndi woposa mfumu. Iye ndi Mulungunso. Taphunzira kale kuti chinthu chodabwitsa kwambiri pa kubadwa kwa Yesu, ndi chakuti Mulungu anakhala munthu. Iye anachita zimenezi mwa Yesu.

Kodi ndi mphatso yotani imene anthu anzeru anaipereka kwa Yesu yomwe inaonetsa kuti Iye ndiye Mulungu?

______________________________________________

==================================================================

12. Mphatso ya libano inaonetsa zimenezi. Yesu anali munthu komanso anali Mulungu. Kodi Mulungu anafuna chiyani kuchokera kwa anthu? Iye amafuna mapembedzo. Iye amafuna kuti anthu azimupembedza mu Mzimu ndi m'choonadi.

Ngati Yesu ali Mulungu, kodi ife timayenera kuchita chiyani kwa Iye?

______________________________________________

==================================================================

13. Ife tiyenera kumupembedza Iye. Yesu ndi Mulungu. Ife sitingathe kumupatsa libano monga anthu anzeru anachitira. Koma tikhoza kumupatsa mapembedzo athu. M'njira imeneyi tikhoza kuonetsa kuti Yesu ndi Mulungu wathu.

Kodi chinthu chodabwitsa kwambiri pa za kubadwa kwa Khristu ndi chiyani?

---

==========================================================================

14. Mulungu anakhala munthu. Ichi ndi chinthu chodabwitsa. Yesu anali Mulungu ndi munthu. Anthu anzeru anaonetsa kuti Yesu anali Mulungu pomupatsa Iye libano.

Mphatso za anthu anzeru zimatikumbutsa ife za kupereka kwa Yesu.

(1) Mmalo mwa golidi wa mfumu, kodi tikhoza kuchita chiyani?
(2) Mmalo mwa libano wa Mulungu, kodi tikhoza kupereka chiyani?
(3) Mmalo mwa mure wa Mpulumutsi wofera, tikhoza kupereka mayamiko

==========================================================================

15. Mmalo mwa golidi wa mfumu tikhoza kukhala omvera. Mmalo mwa libano wa Mulungu, tikhoza kupereka mapembedzo. Ife tikhoza kupereka mphatso monga momwe anthu anzeru anachitira.

Mateyu 2:11:
Namasula chuma chawo, nampatsa Iye mitulo, ndiye golidi ndi libano ndi mure.

Kodi ndi mphatso iti yachitatu imene anthu anzeru anapatsa Yesu?

---

==========================================================================

16. Iwo anapereka mure. Mure analinso mathutsi omwe anali kutengedwa m'mitengo ndipo anali kuumitsidwa. Imeneyi siinali mphatso yachikondwerero yopatsa wina wake. Mure anali mphatso ya munthu amene anali kupita kukafa. Iwo anali kuthiridwa m'mafuta omwe anali kukapaka munthu wakufa Yesu anapakidwa ndi mure atangofa. Pamene anthu anzeru anaona Yesu, nkuti ali mwana wamng'ono. Koma iwo anadziŵa kuti Iye adzakula ndipo tsiku lina adzafa. Iye sadzafa monga anthu ena. Iye ayenera kufera pamtanda kuti apulumutse anthu ku machimo. Mphatso ya mure inalozera imfa yake.

Pamene mngelo anauza abusa za kubadwa kwa Yesu, iye anamutcha Mpulumutsi. Kodi ndi chifukwa chiyani anatcha Yesu "Mpulumutsi?"

---

17. Yesu anatchedwa Mpulumutsi kuonetsa kuti Iye anabwera kudzatipulumutsa. Yesu anadzera anthu onse. Ndipo Iye anabwera kudzafera anthu onse. Iye anabwera kudzapereka moyo wake kufera anthu. Mphatso yachitatu imene anthu anzeru anaiperekayi inalozera imfa monga Mpulumutsi. Mphatso yathu ya kwa Yesu ya imfa yake iyenera kukhala kuthokoza kwathu.

Kodi anthu anzeru anapereka chiyani kuonetsa kuti Yesu adzafa kuti akhale Mpulumutsi wathu?

______________________________

==================================================================

18. Iwo anapereka mure kuonetsa chimenechi. Mure anali wogwiritsidwa ntchito pokwirira maliro. Anaonetsa kuti Yesu adzafa. Ife tidziŵa kuti Iye anafa. Iye anafera pa mtanda chifukwa cha machimo athu. Ife sitingathe kupereka mure kwa Yesu, koma ife tiyenera kumuthokoza chifukwa cha zomwe Iye anachita. Pamene ife tiika chikhulupiriro chathu mwa Yesu, Iye amakhala Mpulumutsi wathu. Ndipo ife tiyenera kumuthokoza nthaŵi zonse.

Kodi lero mwamupatsa Yesu mphatso yakuthokoza? ____________________

____________________________________

==================================================================

19. Tiyenera kuchita zimenezi tsiku ndi tsiku. Ife tiyenera kupatsa Yesu mphatso imeneyi nthaŵi zonse.

Mphatso za anthu anzeru zimatikumbutsa ife kuti tizipereka kwa Yesu.

(1) Mmalo mwa golidi wa mfumu tikhoza kukhala omvera.
(2) Mmalo mwa libano wa Mulungu tikhoza kupereka mapambedzo.
(3) Mmalo mwa mure wa Mpulumutsi wofera, kodi tikhoza kupereka chiyani?

____________________________

==================================================================

20. Tikhoza kupereka kwa Yesu chithokozo. Timayeneranso kumupembedza ndi kumumvera. Mphatso ya anthu anzeru imaonetsa kuti Yesu ndi Mfumu yathu, Mulungu wathu, ndi Mpulumutsi wathu. Ili ndi phunziro labwino lochokera m'nthano ya Khrisimasi. Ukhoza kukhala ulaliki wabwino wa anthu anu.

Ganizirani za zomwe mwaziphunzira lero. Konzani ulaliki wa Khrisimesi wa kwa anthu anu. Patsamba lina lembani zomwe mungadzanene. Onetsani zifukwa zomwe Khristu anabadwira.

===================================================================

21. Tidzaona pepala lanu m'kalasi.

Mphatso za anthu anzeru zimatikumbutsa ife kuti tipereke kwa Yesu:

(1) Mmalo mwa golidi wa Mfumu, kodi tikhoza kuchita chiyani?

(2) Mmalo mwa libano wa Mulungu, kodi tikhoza kuperekanji?

(3) Mmalo mwa mure wa kwa Mpulumutsi wofera, kodi tikhoza kupereka chiyani?

===================================================================

SABATA LACHIWIRI: UKHANDA WA KHRISTU
TSIKU LACHIWIRI: HERODE ANAYESA KUPHA YESU

1. Dzulo tinaona mmene anzeru aku mmaŵa anachezera kwa Yesu. Mphatso za anthu anzeru zimatikumbutsa ife kuperek̩a kwa Yesu:

(1) Mmalo mwa golidi wa Mfumu, tikhoza kuchita chiyani?

_______________

(2) Mmalo mwa libano wa Mulungu, kodi ife tikhoza kupereka chiyani?

_______________

(3) Mmalo mwa mure wa Mpulumutsi wofera, kodi tikhoza kumupatsa chiyani?

_______________

================================================================

2. Pamene tikuganizira za mphatso za anthu anzeru, tiyenera kumumvera, kumupembedza, ndi kumuthokoza. Anthu anzeru anafunsa Mfumu Herode za kumene iwo angamupeze Yesu. Herode ananena kuti iyenso afuna akamupembedze. Koma iye sanathe kutero ayi. Zimenezi ndi zimene tiphunzire lero kwa Herode

(1) Satana anafuna kupha Yesu pofuna kuletsa chikonzero cha chipulumutso.
(2) Kuchokera ku nthano ya Herode timaphunzira kuti mphamvu ya Mulungu ndi yaikulu koposa mphamvu ya Satana.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu 27 mpaka 16. Herode anati iyenso afuna kupembedza Yesu. Kodi kwenikweni iyeyu anafuna kuchita chiyani?

_______________

================================================================

3. Herode ankafuna kupha Yesu. Herode ameneyu anali mfumu ya Ayuda, dziko limene Yesu anabadwira. Iye anali kutchedwa Herode wa mphamvu. Iye anali kuchita zinthu zina zibwino. Iye anamangira Ayuda kachisi wamkulu. Iye anali kusungitsa ntendere pakati pa Ayuda. Koma anali munthu woipa. Iye anapha anthu ambiri. Iye anapha mkazi wake woyamba ndi ana ake aamuna atatu. Iye anachita zimenezi chifukwa anali kuopa kuti angadzatenge malo ake a ufumu. Anzeru aku mmaŵa anadza kwa Herode kufunafuna mfumu yomwe yabadwa tsopano.

Kodi mukuganiza kuti Herode anali kufuna kupha Yesu chifukwa chiyani?

____________________________________________________________

================================================================

4. Tikuganiza kuti Herode anali kuopa kuti Yesu adzamutengera malo ake a ufumu kotero anayesetsa kuti amuphe. Herode anali woipa mtima. Koma kodi uchimo umalowa bwanji m'moyo wa munthu? Satana ndiye amabweretsa uchimo kwa munthu. Pamene munthu avomerezana ndi Satana, Satana amagwira ntchito yake kupyolera mwa munthu ameneyo. Satana anali kugwiritsa ntchito Herode kuti aphe Yesu.

Herode anafuna kupha Yesu. Kodi wina ndani amkafuna kupha Yesu?

____________________

================================================================

5. Satana anafuna kupha Yesu. Iye anadziwa kuti Yesu anabadwa kuti akhale Mpulumutsi. Yesu anabwera kudzatsiriza chikonzero cha Mulungu cha chipulumutso. Satana anafuna kulepheretsa dongosolo la chipulumutso cha Mulungu.

Kodi Satana anafuna kulepheretsa bwanji chikonzero cha chipulumutso cha Mulungu?

__________________________________________________

================================================================

6. Satana anafuna kulepheretsa dongosolo la Mulungu la chipulumutso pofuna kupha Yesu. Iye anayesetsa kupha Yesu pamene anali wamng'ono. Koma khanda Yesu anayenera kukhala ndi moyo. Iye anafunika kuti akhale wamkulu chifukwa iye anabwera kudzafa pamtanda. Kupyolera m'njira yokhayi Iye adakakhoza kutipulumutsa ku machimo athu.

Kodi ndi dongosolo lotani la Mulungu limene Satana anafuna kulilepheretsa?

_____________________________________________

================================================================

7. Satana anafuna kulepheretsa dongosolo la Mulungu la chipulumutso. Satana anadziŵa kuti mphamvu ya Mulungu idzachotsa mphamvu yake. Satana anafuna kulepheretsa dongosolo la Mulungu la chipulumutso pakupha mwana Yesu. Yesu anabwera kudzafa, koma osati ali wakhanda. Iye anadza m'dziko lapansi kuti adzafe pamtanda monga munthu.

Kodi Satana anaphadi khandalo Yesu ndi kulepheretsa dongosolo la Mulungu la chipulumutso?

________________________

==================================================================

8. Satana sanathe kupha Yesu. Mulungu anamuchinjiriza. Mulungu analepheretsa Herode kuti asamupeze Iye ndipo analephera. Kotero Satana sanakhoze kupha Yesu kupyolera mwa Herode.

Kodi ndi chifukwa chiyani Satana anafuna kupha Yesu?

________________________________________________________

==================================================================

9. Satana anafuna kulepheretsa chikonzero cha Mulungu cha chipulumutso. Taona kuti Satana anayesa kupha Yesu kupyolera mwa Herode koma sanathe kuchita zimenezi. Mulungu anauza anthu anzeru kuti asapitirenso kwa Herode. Iwo anapita kwawo podzera njira ina. Mngelo wa Mulungu anauza Yosefe kuti atenge Yesu ndi Mariya kupita nawo ku Aigupto. Iwo anali malo osungika bwino pamene Herode anali kupha ana a m'Betelehemu.

Kodi ndi ndani analepheretsa Satana kuti aphe Yesu?

__________________________________________________

==================================================================

10. Mulungu ndiye amene anachinjiriza Yesu kuti Herode asamuphe. Zimenezi zimatanthauza kuti iye analepheretsa Satana kuti asaphe Yesu. Mulungu anagwiritsa ntchito mphamvu yake posamalira Yesu.

Kuchokera m'nthano imeneyi, ndani ali ndi mphamvu kwambiri? Kodi ndi Mulungu kapena Satana?

________________________

==================================================================

11. Nthano ya Herode imatiphunzitsa ife kuti Mulungu ndi wamphamvu kwambiri. Mulungu anapulumutsa Yesu kuchokera ku mphamvu za Satana. Satana akugwirabe ntchito m'dziko lapansi masiku ano. Iye amayesetsa kutinyenga ife. Iye amayesetsa kutibweretsa ife ku imfa.

1 Petro 5:8:

Khalani odzisungira, dikirani; mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire.

Kodi ndi mphamvu za ndani zimene zili zazikulu kuposa za Satana?

______________________________________________

===========================================================================

12. Mphamvu za Mulungu ndi zoposa. Mulungu ndi wamphamvu. Satananso ndi wamphamvu. Koma Mulungu ndi wamphamvu kuposa aliyense. Mulungu akhoza kukusamalirani inu.

Nthano ya Herode ndi Yesu imatiphunzitsa kuti mphamvu ya Mulungu ndi yoposa ya ndani? __________________________________

===========================================================================

13. Nthano ya Herode ndi Yesu ili ndi phunziro kwa ife. Ikutiphunzitsa ife kuti mphamvu ya Mulungu ndi yaikulu kuposa mphamvu ya Satana. Satana anayesa kupha Yesu. Koma Mulungu anamulepheretsa kuti asachite. M'njira yomweyi, Mulungu akhoza kugwiritsa ntchito mphamvu yake potisunga ife. Satana amayesa kutiononga m'njira zambiri. Iye amatichimwitsa kuti tifulatire Mulungu. Mwina iye amabweretsa ngozi kapena matenda kwa ife. Kapena mwina iye amapangitsa anthu auchimowo kuti atipweteke kapena kutipha.

Kodi ndi chifukwa chiyani Satana anafuna kupha Yesu kupyolera mwa Herode?

______________________________________________________________

________________________________________________________________

===========================================================================

14. Satana anafuna kulepheretsa dongosolo la Mulungu la chipulumutso koma sanathe kuchita zimenezi.

Iye sanathe kupha Yesu kupyolera mwa Herode.

Kodi nthano ya Herode ndi khanda Yesu imatiphunzitsa ife chiyani za mphamvu ya Mulungu?

________________________________________

________________________________________________________

======================================================================

15. Imatiuza ife kuti mphamvu ya Mulungu ndi yaikulu koposa mphamvu ya Satana. Satana safuna kuti ife tikhale opulumutsidwa. Iye safuna kuti ife tizitsata Mulungu. Iye amayesetsa kutibweretsera mavuto ndi kuti-tengera ku imfa.

Pamene Satana akufuna kutiononga ife, kodi mukuganiza kuti tiyenera kuchita chiyani?

____________________________________________

======================================================================

16. Tidzakambirana za zimenezi kukalasi.

Kodi ndi chifukwa chiyani Satana anafuna kupha Yesu kupyolera mwa Herode?

__________________________________________________

________________________________________________________

Kodi nthano ya Herode ndi khanda Yesu imatiphunzitsa ife chiyani za mphamvu ya Mulungu?

________________________________________

________________________________________________________

======================================================================

SABATA LACHIŴIRI: UKHANDA WA KHRISTU
TSIKU LACHITATU: MNYAMATA YESU ANAPITA KU YERUSALEMU

1. Anthu ambiri anali okondwa pamene Yesu anabadwa. Mariya ndi Yosefe anali okondwa. Abusa ndi anthu anzeru anali okondwa. Koma dzulo tinaphunzira kuti mfumu Herode sanali wokondwa. Iye anafuna kupha Yesu.

Kodi ndi chifukwa chiyani Satana anayesa kupha Yesu kupyolera mwa Herode?

___

___

Kodi nthano ya Herode ndi khanda Yesu imatiphunzitsa ife chiyani za mphamvu ya Mulungu?

___

___

==========================================================

2. Satana anafuna kupha Yesu kuti alepheretse dongosolo la Mulungu la chipulumutso koma analephera. Izi zimationetsa kuti mphamvu ya Mulungu ndi yaikulu kuposa mphamvu ya Satana. Yesu anakhala ndi moyo ndipo anakula. Pamene Iye anali ndi zaka khumi ndi ziwiri makolo ake anapita nayenso ku Yerusalemu. Yesu anakhala nthaŵi yaitali ali m'kachisi. Koma potsiriza Iye anabwerera ku mudzi ndi makolo ake. Tiphunzira zinthu ziŵiri zimene Yesu anachita pa moyo wake.

(1) Yesu anaika Mulungu m'moyo mwake kukhala woyamba.
(2) Yesu anamvera makolo ake.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga pa Luka 2:41 kulekeza 52. Ŵerenganinso ndime 41.

Kodi Mariya ndi Yosefe anali kupita kuti chaka ndi chaka?

___

==========================================================

3. Iwo anali kupita ku Yerusalemu. Iwo anali kupita kukapembedza. Iwo anali anthu okhulupirika kwa Mulungu. Iwo anayesetsa kuphunzitsa

Yesu m'njira yabwino. Buku Lopatulika silimatifotokozera zinthu zambiri za umwana wa Yesu. Ilo limanena kuti Mariya ndi Yosefe anapita ndi Yesu ku Aigupto kuthaŵa Herode. Pamene Herode anafa iwo anabwerera ku dziko lakwawo. Iwo anali kukhala m'mudzi wa Nazarete.

Luka 2:52:

Ndipo Yesu anakulabe m'nzeru ndi mu msinkhu, ndi m'chisomo cha Mulungu ndi cha pa anthu.

Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi Yesu poyamba anakula m'chisomo chayani?

______________________________________________

==========================================================================

4. Yesu poyamba anakula m'chisono cha Mulungu. Malo amene Ayuda anali kupembedzera Mulungu anali ku Yerusalemu. Pamene Yesu anali ndi zaka khumi ndi ziwiri anapita ku Yerusalemu ndi mayi ake. Iwo anapita kukachita phwando la paskha. Pa phwando limeneli Ayuda anali kukumbukira mmene Mulungu adapulumutsira anthu awo kuchokera ku ukapolo wa ku Aigupto. Utatha msonkhano Mariya ndi Yosefe anayamba kupita kumudzi. Iwo anapita pamodzi ndi gulu la anansi ndi abwenzi.

Kodi ndani anatsalira kumbuyo m'kachisi ali kulankhulana ndi atsogoleri za Mulungu? ____________________

==========================================================================

5. Yesu ndiye amene anatsalira. Mariya ndi Yosefe ankaganiza kuti Yesu anali pakati pa abwenzi awo. Koma Yesu anatsalira mu Yerusalemu kufikira tsiku limodzi linatha Iye asanaoneke. Ndipo iwo anazindikira kuti Yesu sanali m'gulu lobwerera ku Nazerete. Choncho iwo anabwerera ku Yerusalemu kukamuyang'ana. Ndipo kunawatengera masiku atatu kuti akamupeze.

Luka 2:24:

Ndipo pakupita masiku atatu, anampeza Iye m'kachisi, anali kukhala pakati pa aphunzitsi, namva iwo naŵafunsanso mafunso.

Kodi ndi kuti kumene Mariya ndi Yosefe anapeza Yesu? ____________________

==========================================================================

Kodi mukuganiza kuti Yesu anali kufunsa kapena kulankhulana nawo za chiyani kumeneko? ____________________

---

6. Mariya ndi Yosefe anapeza Yesu ali m'kachisi. Tikuganizira kuti Yesu anali kulankhula ndi kuphunzira za Mulungu. Iye anali pakati pa aphunzitsi kumvetsera ndi kumafunsa mafunso. Anthu anali kudabwa naye pakumvetsetsa kwake.

Luka 2:48-49:

> Ndipo amake anati kwa Iye, "Mwanawe, wachitiranji ife chotere; atate wako ndi ine tinali kufunafuna iwe ndi kuda nkhaŵa. Ndipo Iye anati kwa iwo, "kuli bwanji kuti munali kundifunafuna Ine? Simunadziŵa kodi kuti kundiyenera Ine ndikhale mnzake za Atate wanga?"

Taganizirani za zimene Yesu ananena. Kodi Yesu anaganizira kuti anachita china chake cholakwa? ____________

---

7. Yesu anali wodabwa. Iye sanaganize zakuti wachita kanthu kena kolakwa. Iye anati; "Simunadziŵa kodi kuti kundiyenera Ine ndikhale mnzake za Atate wanga?" Kodi Yesu anali kuti pamene ananena za zimenezi. Kodi Iye anali mnyumba ya Yosefe? Ayi. Iye anali m'kachisi. Kachisi anali malo amene Ayuda anali kupembedzeramo Mulungu. Iwo anali kuitcha kuti ndi, "Nyumba ya Mulungu." Yesu anaitcha kuti ndi "Nyumba ya Atate wanga."

Kodi Yesu anaganiza kuti Atate ake weniweni ndani? ____________

---

8. Iye anadziŵa kuti Mulungu ndiye atate wake woona. Yesu anali kukhala ndi Yosefe ndi Mariya. Iwo anali makolo ake a padziko lapansi. Koma Atate ake weniweni anali Mulungu. Iye anadziŵa kuti poyamba m'moyo mwake ayenera kutenga Mulungu kuti akhale oyamba. Chinthu chimenechi ndicho choyamba chimene tikuchiphunzira kuchokera pakachezedwe ká Yesu ku Yerusalemu.

Pa nthaŵi imeneyi, kodi Yesu anaonetsa bwanji kuti amaika Mulungu kukhala woyamba m'moyo mwake? ______________________

==========================================================================

9. Yesu anatsalira m'kachisi. Yesu anali wamng'onobe. Iye anali ndi zaka khumi ndi ziŵiri zokha. Makolo ake anali ofunikabe kwa Iye chifukwa anali kukhala nawo, ndipo anali kumusalira. Koma Iye anadziŵa kuti sakadayenera kuŵaika iwo kukhala oyamba m'moyo mwake. Zinthu zomwe Iye anachita ku Yerusalemu zinaonetsa zimenezi.

Lembani chinthu choyamba chimene taphunzira kuchokera paulendo wa Yesu wokacheza ku Yerusalemu.

(1) ______________________

(2) Yesu anamvera makolo ake.

==========================================================================

10. Kuchokera pa kukacheza ku Yerusalemu tikuphunzira kuti Yesu anaika Mulungu m'moyo mwake kukhala woyamba. Iye anachita zimenezi pamene anali wamng'ono. Iye anali ndi zaka khumi ndi ziŵiri zokha. Achinyamata athunso masiku ano akhoza kusankha kuchita zimenezi. Iwo akhoza kuika Mulungu kukhala woyamba. Iye tiyenera kuŵaphunzitsa kuti achite zimenezi ndipo ifenso tiyenera kuchita zimenezi.

Koma pali kanthu kena kachiŵiri kamene takaphunzira kuchokera m'ndime zimenezi. Yesu atatha kunena kuti Iye ayenera kukhala mnzake za Atate wake, timaŵerenga mawu aŵa.

Luka 2:51:

> Ndipo anatsika nawo pamodzi nadza ku Nazarete;
> nawamvera iwo: ndipo amache anasunga zinthu izi zonse
> mumtima mwake.

Pa ndime imeneyi, kodi Yesu anamvera yani? ______________________

==========================================================================

11. Iye anamvera Mariya ndi Yosefe. Iye anamvera makolo ake. Iye anaika Mulungu kukhala woyamba m'moyo mwake. Iye anadziŵa kuti ayenera kuchita chifuniro cha Mulungu m'zinthu zonse. Koma Iye anamveranso makolo ake. Patapita nthaŵi Yesu anasiya makolo ake. Iye anali kuyendayenda nalalikira, kuphunzitsa ndi kuchiritsa. Iye anamvera makolo a dziko lapansi ngakhale kuti Iye anali Mwana wa Mulungu.

Ngati ana a Chikhristu atsata chitsanzo cha Yesu, kodi iwo adzachita chiyani kwa makolo awo?

____________________

---

12. Iwo adzaŵamvera. Yesu anapereka chitsanzo kwa ana a Chikhristu achinyamata. Iwo ayenera kumvera makolo awo chifukwa iwo amaganiza kuti ayenera kungochita chofuniro cha Mulungu chokha. Komanso ndi chifuniro cha Mulungu kuti ana azimvera makolo awo. Ana ena amaganiza kuti amadziŵa zinthu zambiri koposa makolo awo. Nkutheka kuti iwo anaphunzira zinthu zina ku sukulu zimene makolo awo sazidziŵa. Koma makolo awo ali ndi nzeru chifukwa chakukhalitsa ndi moyo.

Aefeso 6:1:

> Ananu, mverani akukubalani mwa Ambuye, pakuti ichi nchabwino.

Kodi Yesu anachita chiyani kwa makolo ake? ____________________

---

13. Iye anamvera makolo ake. Yesu anatsata chifuniro cha Mulungu. Iye anaika Mulungu kukhala woyamba m'moyo mwake. Koma Iye anamveranso makolo ake a dziko lapansi. Timaphunzira zinthu zonsezi m'ndime zonena za Yesu, ali ku Yerusalemu.

(1) Yesu anaika Mulungu kukhala woyamba m'moyo mwake.
(2) Yesu anamvera makolo ake.

Ngati ana a Chikhristu atsata chitsanzo cha Yesu, kodi iwo adzamvera yani?

____________________

---

14. Iwo adzamvera makolo awo. Koma iwo, monga Yesu ayenera kutenga Mulungu kukhala woyamba. Makolo onse si Akhristu. Ndiponso makolo a Chikhristu amalakwa. Nthaŵi zina makolo amauza ana kuti achite zinthu zomwe siziri zabwino. Kapena mwina iwo amafuna ana awo kuti azichita zinthu zomwe sizingaike Mulungu kukhala woyamba m'miyoyo mwawo. Ana Achikhristu ayenera kuonetsa kuti amaika Mulungu kukhala woyamba.

Kodi ndi chinthu chachiŵiri chiti chimene tachiphunzira kuchokera pakucheza kwa Yesu ku Yerusalemu?

(1) Yesu anaika Mulungu kukhala woyamba m'moyo mwake.
(2) ______________________________

==========================================================================

15. Yesu anamvera makolo ake. Yohane anali mnyamata wa Chikhristu amenenso anayesa kutsata chitsanzo cha Yesu. Iye anayesetsa kumvera makolo ake. Koma pamene Yohane anakula msinkhu anakhulupirira kuti Mulungu ali kumufuna kuti akhale mbusa Makolo ake anafuna kuti iye akagwire ntchito mumzinda kuti azikalandira ndalama zambiri. Koma Yohane anati, "Ayi," ine ndayesetsa kukumverani nthaŵi zonse koma tsopano ndadziŵa kuti Mulungu akufuna kuti ndikhale mbusa. Chifukwa cha chimenechi ine ndiyenera kukhala mbusa.

Kodi Yohane anaika ndani m'moyo mwake kukhala woyamba? ______________

==========================================================================

16. Yohane anaika Mulungu kukhala woyamba. Tiyeni tiphunzitse ana athu kuchita zimenezi.

Kodi kucheza kwa Yesu ku Yerusalemu pamene anali wa zaka khumi ndi ziwiri kumatiphunzitsa chiyani za Iye?

(1) ______________________________

(2) ______________________________

SABATA LACHIŴIRI: UKHANDA WA KHRISTU
TSIKU LACHINAYI: NTCHITO YA YOHANE MBATIZI

1. Dzulo tinaona za kucheza kwa Yesu ku Yerusalemu. Tinaona zimene zinaoneka pamene Iye anali ndi zaka khumi ndi ziŵiri.

Kodi kucheza kwa Yesu ku Yerusalemu pamene anali ndi zaka khumi ndi ziŵiri kumatiphunzitsa chiyani za Yesu?

(1) ______________________________

(2) ______________________________

===========================================================

2. Kucheza kumenek kumatiphunzitsa kuti Yesu anaika Mulungu kukhala woyamba m'moyo mwake. Timaphunziranso kuti Iye anamvera makolo ake. Timangodziŵa kokha kuti Yesu anakacheza ku Yerusalemu pamene Iye anali kukula. Koma Buku Lopatulika limatiuza za munthu wina amene anali kukulanso pa nthaŵi imeneyi. Munthu ameneyu anali Yohane Mbatizi. Inali ntchito ya Yohane Mbatizi kukonza njira ya Khristu. Izi ndizo zimene tiphunzire za Iye.

(1) Yohane Mbatizi anauza anthu kuti alape ndi kukonza khwalala la Khristu.

(2) Yohane Mbatizi amatiphunzitsa ife kukhala odzichepetsa pochitira umboni za Khristu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika muŵerenge pa Mateyu 3:1 mpaka 12, kodi uthenga wa Yohane Mbatizi unali wotani?

______________________________

______________________________

===========================================================

3. Yohane Mbatizi anauza anthu kuti alape. Izi zimatanthauza kuti iwo adayenera kutembenuka kusiya machimo awo. Yohane Mbatizi anabadwa msanga miyezi khumi ndi isanu ndi umodzi Yesu asanabadwe. Mayi wake anali Elizabeth. Iye anali wa pfuko la Mariya. Bambo a Yohane anali Zakaliya, wa nsembe wa m'kachisi koma anali wokalamba. Iwo sanali kuganiza kuti angaone mwana. Koma mngelo anadza kwa Zakariya ndi kunena kuti iwo adzakhala ndi mwana wa mwamuna. Mwana wao adzakhala wodzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ndipo zinachitika monga momwe mngelo ananenera. Pamene

Yohane anakula, Iye anali kulalikira kumphepete kwa mtsinje wa Yordani. Iye anali kubatizanso anthu mu mtsinjemo.

Kodi ndani anatumiza Yohane Mbatizi kuti akakonze njira ya Khristu?

______________________________

================================================================

4. Mulungu ndiye anamutumiza iye. Mulungu anauza Yesaya m'Chipangano Chakale kuti Yohane adzabwera. Yohane anauza anthu kuti alape. Anthu ena anali kuganiza kuti Yohane anali munthu wamisala. Iye anali kukhala m'chipululu. Iye ankavala chovala chodabwitsa chopangidwa ndi ubweya wa nyama. Iye anali kudya dzombe ndi uchi. Koma Yohane sanali munthu wamisala. Iye anali mneneri wotumidwa ndi Mulungu. Yohane anali ndi ntchito yofunika kwambiri.

Mateyu 3:3:

> Mawu a wopfuula m'chipululu, konzani khwalala la
> Ambuye, lungamitsani njira zake.

Kodi Yohane anali kukonza njira ya ndani? ____________________________

================================================================

5. Iye anali kukonza njira ya Ambuye. Iye anali kukonza njira ya Khristu. Mu nthaŵi zakale ngati mfumu ikufuna kukacheza poyamba inali kutumiza mthenga. Masiku anonso timachita chimodzimodzi. Munthu wa uthenga amauza anthu kuti mfumu ili kubwera. Iye amauza anthu kuti akonze msewu. Iwo amayenera kukwirira maenje a mumsewu. Iwo ayenera kuchotsa mokhotakhota ndi kuongola malo ena.

Kodi ndi ndani anabwera kudzauza anthu kuti alape ndi kulungamitsa njira ya Khristu?

______________________________________________

================================================================

6. Yohane Mbatizi anakonzera Khristu njira. Koma iye sanauze anthu kuti akwirire maenje m'misewu. Iye sanaŵauze kuti alungamitse misewu yokhota. Iye anaŵauza kuti akonze mitima yawo kukonzekera Yesu.

Kodi iye anaŵauza kuti achite chiyani kuti akonze mitima yawo pokonze-

kera Khristu?

___________________________________________

================================================================

7. Yohane Mbatizi anauza anthu kuti alape. Iye anaŵauza iwo kuti atembenuke ku machimo awo. Anthu ambiri anabwera kudzamva zonena za Yohane. Yohane anaŵauza kuti akonzere Khristu njira.

Mateyu 3:5-6:

Pamenepo panamtulukira iye aku Yerusalemu, ndi Yudeya lonse, ndi dziko lonse loyandikana ndi Yordano; nabatizidwa ndi iye mu mtsinjewo wa Yordano, alikuulula machimo awo.

Kuchokera pa ndime imeneyi, kodi Yohane anachita chiyani kwa anthu pamene iwo analapa?

___________________________________________

================================================================

8. Iye anaŵabatiza. Zimenezi zinaonetsa kuti iwo analapadi. Ndi anthu ambiri anabwera kudzamva Yohane ali kulalikira. Yohane anaŵauza iwo kuti akonzere Khristu njira. Yohane sanaŵauze kuti akwirire maenje kapena kukonza misewu.

Iye asanaŵabatize iwo, kodi Yohane anauza anthu kuti achite chiyani pokonzekera Khristu?

___________________________________________

================================================================

9. Iye anaŵauza kuti alape. Ntchito ya Yohane inali yokonza njira ya Khristu kuti abwere. Ntchito ya Yohane inali yofunika kwambiri. Iye anali munthu wamphamvu koma kodi Yohane anafunsa anthu kuti amuyamikire? Ayi! Yohane Mbatizi anali munthu wodzichepetsa kwambiri. Taonani zimene iye anauza anthu.

Mateyu 3:11:

Inetu ndakubatizani inu ndi madzi kuloza kukutembenuka mtima; koma Iye wakudza pambuyo panga, ali wakundiposa mphamvu, amene sindiyenera kunyamula nsapato zake; Iyeyu adzakubazani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto.

Kodi Yohane anaganiza kuti ndani a[illegible] wamphamvu, iye mwini kapena Khristu?

---

10. Yohane anadziŵa kuti Khristu anali wamphamvu. Iye anauza anthu zimenezi. Yohane anali ndi ntchito yofunika kwambiri, koma iye anadziŵa kuti Khristu anali wofunika koposa. Yohane sanali kuganiza kuti iye anali wabwino kotero kuti adakakhoza kunyamula msapato za Yesu. Kunyamula msapato za munthu inali ntchito ya kapolo. Yohane anadziona kuti iye sanali woyenera kukhala kapolo wa Khristu. Yohane anali mboni yodzichepetsa ya Khristu.

Ngati ife titsata chitsanzo cha Yohane, kodi tidzakhala mboni zotani? Kodi tidzakhala onyada kapena mboni zodzichepetsa?

---

11. Tidzakhala odzichepetsa. Nthaŵi zina anthu amene ali kugwirira ntchito Khristu amaganizira kuti iwo ndi wofunika koposa. Alaliki ndi ofalitsa uthenga ena amaganiza kuti ndi anthu a akulu. Iwo amafuna kuti anthu aziŵayamikira ndi kuŵalemekeza. Koma zimenezi sizabwino ayi. Ndi zoona kuti kuchitira umboni za Khristu ndi ntchito yofunika koposa. Koma tiyenera kufuna kulemekeza Khristu, osati kudzilemekeza tokha. Tiyenera kukhala mboni za Khristu zokhulupirika.

Kodi mphunziro ili ndi ndani amene ali mboni ya Khristu yodzichepetsa?

---

12. Yohane Mbatizi ndiye chitsanzo chimenechi. Iye sanafune kulemekezedwa. Iye anafuna kuti anthu akonzekere kulandira Khristu. Iye anali ndi ntchito yaikulu. Khristu ananena za iye kuti.

Mateyu 11:11:

> Indetu ndinena kwa inu, Sanauke wakubadwa mwa akazi munthu wamkulu woposa Yohane Mbatizi; koma iye amene ali wochepa mu Ufumu wa Kumwamba amkulira iye.

Kodi Yohane Mbatizi anauza anthu kuti achite chiyani chokonzekera kulandira Khristu?

______________________________

===========================================================================

13. Iye anaŵauza kuti alape. Iye anakhala chitsanzo chabwino kwa ife.

Kodi ndi umboni wa chitsanzo chotani umene Yohane Mbatizi amatiphunzitsa kuti tikhale?

______________________________

===========================================================================

14. Yohane Mbatizi amatiphunzitsa ife kuti tikhale mboni zodzichepetsa. Timafuna anthu kuti aziona Khristu osati ife. Izi ndizo zimene Yohane Mbatizi anazifuna. Iye anali mboni ya Khristu yokhulupirika. Nachi china chimene iye ananena za Khristu.

Yohane 3:30:

Iyeyo ayenera kukula koma ine ndichepe.

Kodi muli kuganizira kuti alaliki ndi ena ofalitsa mawu ndi odzichepetsa?

______________________________

Kodi ndi chiyani chimene chingaŵathandize iwo? ______________________________

===========================================================================

15. Tidzakambirana za zimenezi tonse.

Iye asanaŵabatize, kodi Yohane Mbatizi anauza anthu kuti achite chiyani pokonzekera Khristu?

______________________________

Kodi ndi umboni wachitsanzo chotani umene Yohane Mbatizi amatiphunzitsa kuti tikhalire?

______________________________

===========================================================================